



ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027

UNDUNA WA ZACHILENGEDWE
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo


THYOLO
DISTRICT

Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezereka kukhudzidwa ndi El Nino wa mphamvu. El Nino ndi kutentha koposera muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse lapansi.

Boma la Thyolo likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika komanso yochepera apo mu nyengo ya mvula ya 2026/2027.


October 2026



Madera ambiri kudzakhala nyengo yotentha komaso yopanda mvula m'mweziwu.

Komabe pali kuthekera kolandira mvula ya Chizimalupsya yomwe idzabwere ndi mphepo ya mkuntho m'madera ena.


November 2026



Tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika m'mweziwu.


Madera ambiri akuyembekezereka kudzalandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm yomwe idzakhale ya mabingu ndi ya mphepo ya mkuntho.

December 2026




M'mwezi wa December, madera ambiri ali ndikuthekera kolandira mvula ya mlingo okhadzikika wa pakati pa 200mm ndi 250mm. Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kudzayamba sabata lachiwiri m'mweziwu.

January 2027



Tiyembekezere mvula ya mlingo wokhazikika komanso yocheperapo ya mlingo wapakati pa 150mm ndi 200mm m'mweziwu. Pali chiopsezo cha ng'amba ya sabata imodzi m'mweziwu.


February 2027



Tiyembekezere mvula yochepera mlingo okhazikika m'mweziwu. Madera ambiri akhoza kudzalandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm.


Pali chiopsezo cha ng'amba yopyola sabata imodzi m'mweziwu.

March 2027



Mvula ya mlingo okhazikika, komanso kuposera apo ya mlingo wa 150mm ndi 200mm ikuyembekezereka m'madera ambiri m'mweziwu. Mvula ya mlingo oposera 250mm ikuyembekezereka m'madera ochepa monga Luchenza town, TA Nchilamwela, TA Chimaliro ndi TA Kapichi.

April 2027



M'mweziwu, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera apo. Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm ikuyembekezereka m'madera ambiri.

Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April

DZINJA MWACHIDULE

Kuyamba kwa mvula yokhazikika

Ikuyembekezereka sabata lachiwiri ya mwezi wa December 2026.

Ng'amba

Pali chiopsezo cha ng'amba ya sabata imodzi m'mwezi wa January komaso yoposera sabata imodzi m'mwezi wa february.


Kutalika kwa nyengo ya dzinja

Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 110 ndi 120.

Mathero a mvula dzinja

Ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April

MONTH	NORMAL RANGE	FORECAST
OCT	13.1-36.8	25.6
NOV	66.6-109.2	69.4
DEC	155.7-279.6	244.5
JAN	227.5-343.9	216.4
FEB	182.6-289.9	136.0
MAR	111.8-237.0	202.8
APR	46.8-95.2	80.2



Tebulo ndi galafu zili pamwambapa zikuonetsa kagwedwe ka mvula ku Thyolo.

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61



metdept@metmalawi.gov.mw



www.metmalawi.gov.mw